

**Maphunziro**  
a  
**Alangizi othandizira**  
**alimi a ziweto m'midzi**


**Mbuzi**  
**ndi nkhosa**

Small Scale Livestock and Livelihoods Program  
PO Box 1604, Lilongwe Malawi



# Mbuzi ndi nkhosa

## Phunziro 1: Kawetedwe ka mbuzi ndi nkhosa



Zolinga za phunziroli:

Pomaliza pa phunziro ili wophunzira athe:

1. Kumvetsa kufunika kwa mbuzi muno m'Malawi
2. Kudziwa zimene zimabvuta pa kawetedwe kambuzi
3. Kufotokoza njira zosiyanasiyana za kawetedwe mbuzi muno m'Malawi
4. Kudziwa kufunika kwake kosamalira mbuzi mwanjira za makono
5. Kufotokoza njira zina za kasamalidwe kambuzi zosiyana ndi zimene zilipo panopa

### Yankhani mafunso awa:

Fotokozani zifukwa zimene alimi amawetera mbuzi. (aliyense afotokoze zifukwa zowetera mbuzi m'dera la kwao.)

Lembani m'ndandanda wa zifukwa zowetera mbuzi kuyambira chofunika kwambiri ndi kumatsika. Zina mwazifukwa ndi izi:

- Zongonyaditsa
- Zogwiritsa ntchito pamiyambo yosiyanasiyana
- Kopezera ndalama
- Chuma cha pakhomo
- Nyama
- Mkaka
- Zikopa ndi zikumba
- Manyowa owonjezera chonde m'nthaka

**Yankhani mafunso awa:**

Fotokozani mabvuto okhudzana ndi kawetedwe ka mbuzi ndi m'mene mungathetsere mabvuto amenewa. Ena mwa mabvutowa ndi awa:

- Malo a mudzi (a gulu)
- Kusankha ziweto zoswanitsa chisawawa
- Kuweta mbuzi m'makola osayenera
- Bvuto la katetezedwe kamatenda maka nyengo ya mvula
- Bvuto la kadyetsedwe
- Kusowa kwa misika yolongosoka
- Kutangwanika ndi mbewu zina za m'munda
- Kubedwa kwa mbuzi
- Kujiwa kwa mbuzi makamaka zomangirira pachingwe kutchire

**Yankhani mafunso awa:**

Fotokozani ubwino wa kawetedwe kambuzi ndi nkhoa ku kumudzi poyerekeza ndi kawetedwe kaziweto zina. Wina mwa ubwino wakawetedwe kambuzi ndi nkhoa poyerekeza ndi ziweto zina ndi:

- Sizifaifa nthawi ya chirimwe
- Sizibvuta kudyetsera popeza mbuzi zimadya zitsamba osati msipu kwenikweni ayi
- Mbuzi ndi zopirira kumatenda ndi nyongolotsi/njoka za m'mimba kusiyana ndi nkhoa
- Sizibvuta kusamala chifukwa chakuchepa msinkhu.
- Zikajiwa kapena kubedwa siziwawa kwenikweni popeza ndi chiweto chochepa msinkhu kusiyana ndi ng'ombe
- Zimatetha kwambiri - zimabereka ana a mapasa nthawi zambiri, ndipo zimaberekana pafupipafupi.
- Mtengo wogulira ndi wochepe. Zikajiwa kapena kubedwa siziwawa kwenikweni.
- Ndalama zolowa ku mankhwala wochizira ndi katemera ndi za zakudya ndi zochepe polinganiza ndi za ng'ombe.

**Njira za kawetedwe ka mbuzi:**

Kawetedwe	Machitidwe ake
Ka kumudzi	<p>Amalola mbuzi kukadya kuli konse - kungozitaya. Amasamala ndi anthu a pabanjapo. Amazipatsanso zotsala za kukhitchini kapena za mbeu za kumunda.</p> <p>Mbuzi amazimangirira pa chingwe nthawi ya mvula poteteza mbeu za kumunda ndi kuzitaya nthawi ya chirimwe.</p>
Kudyetsera m'khola ndi kutayira.	<p>Kasamalidwe aka ndi kapakatikati pa kutayira ndi kudyetsera m'khola.</p> <p>Zimaloledwa kudya kutchire ndiponso kudyetsera m'khola malingana ndi nthawi, anthu amadyetsera ndi zakudya zimene zilipo. Mbuzi zimaloredwa kukadya msipu/zitsamba kwa maora anai kapena asanu ndi limodzi tsiku ndi tsiku. Ndipo amazitsekera m'khola momwe amazipatsa msipu ndi masamba. Izi ndi zochitika nthawi ikapezeka.</p>
Kudyetsera m'khola	<p>Kawetedwe aka ndi koyenera komwe kulibe malo okwana komwe mbuzi zingathe kukadya msipu. Ndi kawetedwe koyenera mbuzi zomwe zilipo pang'ono ndi kumene kulibe malo okwana.</p> <p>Mbuzi sizituluka m'khola ndipo zimadyera m'khola momwemo. Njira ya kawetedwe aka ndi yabwino chifukwa mlimi atha kusankha tonde wokakwera misoti ndi mathadzi ndi nthawi yoti ziyambe kuberekana.</p> <p>Kawetedwe aka kamalira ntchito ndi nthawi yambiri ndi ndalama zambiri zomangira khola, kugula zakudya, mankhwala ndi kulipira a ntchito. Atonde, ana ndi mikota zizitsekeredwa m'makola osiyana.</p>

## Phunziro 2: Mitundu ya makola a mbuzi

**Zolinga za phunziroli:**

**Pomaliza pa phunziro ili wophunzira athe:**

1. Kumvetsa ndi kufotokoza za makola asiyanasiyana ambuzi kuphatikizapo makola apansi ndi a m'mwamba (omangira mitengo kapena matabwa)

### **Mitundu ya makola a mbuzi ndi nkhosa:**

- **Makola a m'mwamba:** Makola awa amamangidwa ndi mitengo pamwamba pamphanda ndipo paphaka pamaikidwa mitengo yaraundi bwino mosiya timipata ting'onoting'ono takuti chiboda chambuzi sichingalowe, koma poti ndowe zake zizigwera pansu. Mbuzi zimachita bwino m'makola otere. Kuipa kwa makola awa ndi kwakuti ndi ofuna ndalama zambiri zogulira matabwa, misomali; koma ndi abwino kwa mbuzi. Ikani mphasa kapena tsekera m'mbali mwa zikupa za khola poteteza mbuzi ku mphepo ya mkuntho.
- **Makola omangidwa ndi njerwa:** Makola awa ndi omangidwa ndi njerwa zotentha ndipo ndi okwera mtengo koma ndi okhalitsa.
- **Makola a m'dindo:** Makola awa ndi a ndendera kapena a ngomi malingana ndi m'mene mlimi wafunira. Kamangidwe kake ndi monga momwe amamangira nyumba zakumudzi. Makola awa ndi osabvuta kumanga ndipo zipangizo zake zimapezeka kumudzi komweko pamtengo wotsika.


### **Kusankha malo omangapo khola**

- Likhale kufupi ndi nyumba ya mlimi ngati kumaloko kuli umbabva wochuluka.
- Khola likhale pamalo popanda lowe kapena pamene pamadikha madzi nthawi ya mvula.

### **Milingo (miyeso) ya makola:**

- Kukula kwa khola kutengera ndi kuchuluka kwa mbuzi zomwe mlimi akufuna kuweta.
- Mbuzi imodzi imafuna malo akwanira theka la mkono mbali zonse (**0.5 square metres per adult goat**).


Kuchuluka kwa mbuzi	Kukula kwa malo	Khola la ngomi	Khola ndendera
Kuchokera pa mbuzi imodzi kufika khumi	Mikono isanu mbali zonse (5m <sup>2</sup> )	Mikono iwiri mulifupi ndi mikono iwiri ndi theka mulitali	Mikono iwiri ndi theka kudutsa pakati ndi pakati
Kuchokera pa mbuzi khumi ndi imodzi kufika makumi awiri	Mikono khumi mbali zonse (10m <sup>2</sup> )	Mikono itatu mulifupi ndi mikono itatu ndi chikhatho mulitali	Mikono itatu theka n'chikhatho kudutsa pakati ndi pakati
Kuchokera pa mbuzi makumi awiri kufika pa mbuzi makumi atatu	Mikono khumi ndi isanu mbali zonse. (15m <sup>2</sup> )	Mikono itatu mulifupi ndi mikono isanu mulitali	Pafupifupi mikono inayi ndi theka kudutsa pakati ndi pakati.



Khola lambuzi lapansi



Khola lambuzi lam'mwamba



- Sesani m'khola pafupi pafupi kuti ndowe zisachuluke. Ndowe ziunjikidwe pamodzi kuti zigwiritsidwe ntchito yothira kumunda ngati manyowa.

- Mukhoza kuphatikiza ndowe kuzotsala za ku mbewu, udzu ndi zina zosesedwa pakhomo ndi kupanga manyowa a mnkhuti kapena a chimato abwino zedi.
- Denga la khola la mbuzi likhale losadontha. Ngati likudontha, konzani mwansanga, denga lakhola likhale lotsetsereka moyenera (30°).
- Tipewe kugwiritsa ntchito mapepala a pulasitiki pofolera denga chifukwa likakhalitsa limanyotsoka. Kuli bwino kufolera ndi udzu wokwana ndipo denga litsetsereke ndi madigiri 30 kuti lizitaya madzi a mvula. Pulasitiki akakhalitsa amanyotsoka ndiye mbuzi ikadya imadwala kapena kufa.
- Khomani mbalawala mkati mwa nkomo osati kunjira ayi. Mbuzi sizingazule mbalawala ngati zigunda mbalawala.

### **Phunziro 3: Zakudya ndi kadyetsedwe kambuzi**

**Zolinga za phunziroli:**

**Pomaliza pa phunziro ili wophunzira athe:**

- 1. Kudziwa zakudya zoyenera kuphatikiza popanga zakudya zamagulu zopatsa mbuzi kuonjeza pa msipu ndi masamba**
- 2. Kudziwa zakudya zoonjezera zodyetsa mbuzi**

**Yankhani mafunso awa:**

Fotokozani m'mene alimi amadyetsera mbuzi zawo pa nyengo zosiyanasiyana za mchaka. Kadyetsedwe kambuzi kakusiyana bwanji ndi kadyetsedwe ka nkhosa ndi ka ng'ombe?

- Mbuzi ndi nkhosa zimasiyana kadyedwe. Nkhosa zimadya chimodzimodzi ngati ng'ombe - zimakonda kudya msipu wa udzu, pamene mbuzi zimadya zophatikiza, masamba a mitengo ndi zitsamba. Mbuzi imatha kusankha nsonga zophuka kumene za mitengo ndi zitsamba ndi mbali zina zokonedwa za zomera.
- Mbuzi zimapirira nthawi yachirimwe kusiyana ndi ng'ombe ndi nkhosa.
- Koma nthawi ya mwamvu, mbuzi sizisangalala monga m'mene zimapezera bwino ng'ombe ndi nkhosa. Mbuzi sizisangalala makamaka pamene zimakhala pachingwe nthawi ya mwamvu. Ndi koyenera kuzipatsa zakudya zoonjezera nthawi ya mwamvu. Zakudya zoonjezera zomwe zimapezeka m'Malawi muno ndi monga izi:
  - Madeya/Gaga
  - Mankhupete a mpunga
  - Masangwe, Chigwada, Kholowa ndi mitsitsi yake
  - Zotsala za ku khitchini
  - Zibalobalo za msangu. Perekani theka la kilo patsiku kwa mbuzi ya bere; ku zibalobalo kumachokera chakudya chokulitsa.
  - Masamba a mitengo yomwe mbuzi zimadya; muyenera kuika mgome kuti zisakhudzane ndi ndowe kapena mkodzo.



**Chitsanzo cha kasakanizidwe ka chakudya cha magulu:**

Madeya a chimanga kapena a mpunga (Zopatsa mphamvu)	6.9 Kg (69%)
Masamba a lukina ndi zibalo zake (Zokulitsa)	3.0 Kg (30%)
Mchere	0.1 Kg (1%)
<b>Zonse pamodzi</b>	<b>10 Kg (100%)</b>
Kudyetsa kwake: Perekani chakudya chosakanizachi chochuluka ndi 0.7kg kufika pa 1.0 kg pa mbuzi ili yonse pa tsiku.	

## Phunziro 4: Kukweretsa mbuzi ndi nkhosa



Zolinga za phunziroli:

Pomaliza pa phunziro ili wophunzira athe:

1. Kudziwa mitundu ya nkhosa ndi mbuzi zomwe zimapezeka muno m'Malawi ndi kaonekedwe kake
2. Kudziwa zofunikira pa kabereketsedwe ka mbuzi
3. Kudziwa za m'mene mbuzi za chikuda amazisinthira mtundu kuti zikhale za misinkhu ikuluikulu

### Yankhani mafunso awa:

Tchulani mitundu ya mbuzi ndi nkhosa zopezeka m'Malawi ndi kunena ubwino ndi kuipa kwake kwa mtundu uli wonse. Zina zomwe zalembedwa m'musimu zikhoza kukuthandizani:

Mtundu wa mbuzi	Ntchito ndi ubwino wake
<p>Yachikuda</p> 	<p>Nyama. Uwu ndi mtundu wambuzi womwe umawetedwa kwambiri muno m'Malawi.</p>
<p>Boer</p> 	<p>Nyama. Uwu ndi mtundu umene umagwiritsidwa ntchito pofuna kukuza mtundu wa mbuzi za chikuda pokweretsa zachikuda ndi ma boer.</p>

<p>Saanen</p> 	<p>Mkaka ndi nyama. Zimawetedwa pofuna kukhala ndi mbuzi zokama mkaka.</p>
<b>Nkhosa</b>	<b>Ntchito ndi ubwino wake</b>
Nkhosa za chikuda	Za nyama
Nkhosa za mtundu wa Dorper	Za nyama. Zimawetedwa chifukwa ndi za zikulu misinkhu ndipo ndi za nyama yambiri. Koma sizochuluka muno m'Malawi.

### Kabereketsedwe ka mbuzi:

**Yankhani mafunso awa:**

Kodi msoti wa mbuzi umatha msinkhu ukakwana miyezi ingati?

Nanga zizindikiro za nyere zimatenga nthawi yaitali bwanji?

Ngati mbuzi sinakweredwe pomwe inali ndi nyere, pamatenga masiku angati kuti ikhalenso ndi nyere ina?

Nanga bere la mbuzi limakhala la miyezi ingati?

Nanga mbuzi ikayamba nyere imaonetsa zizindikiro zotani?

## Kabereketsedwe ka mbuzi:

Masiku a pakati pa nyere ndi nyere ina	Pakati pa masiku 18 ndi 20
Kutalika kwa nthawi yomwe nyere imatenga	Pakati pa maora 24 ndi 36
Masiku amene bere limatenga	Masiku 150 (miyezi 5)
Kuchuluka kwa ana pakuswa kwa kamodzi	M'modzi kapena awiri
Kutha msinkhu: Tonde Msoti	Pakati pa miyezi 8 kapena 9 Miyezi 7

## Zizindikiro za nyere ya mbuzi:

- Kuliralira
- Kukweteza mchira
- Maliseche amaoneka ngati atupa (kutota) ndipo amafilirika
- Kumaliseche kumatuluka chikazi choyera ngati madzi adzira loyera
- Chilakolako cha chakudya chimachepa
- Imakodzakodza
- Nyere ikamayamba kumene mbuziyo imakwera zinzake, koma nyere ikafika pachimake, imalolera kukweredwa ndi zinzake.
- Pakakhala tonde wankulu, amamemesa mbuzi yomwe ili ndi nyereyo.

## Kusankha mbuzi zofunika kukweretsa ndi kuswanitsa:

- Kusankha ndi ntchito yosankha mbuzi zooneka bwino pa zimene zilipo kuti zikhale makolo a mbuzi za mtsogolo. Mchitidwe wosankha mbuzi zofunika kukweretsa ndi wabwino ngakhale sutsatidwa muno m'Malawi. Posankha a tonde tionetsetse kuti ali ndi msinkhu wozuka bwino, a thanzi, ndi okula mofulumira. A tonde omwe ndi osaoneka bwino athenedwe (afulidwe), agulitsidwe kapena aphedwe. Ngati tichita izi, tidzaona kusintha kwa bwino kwa mbuzi za mtsogolo.
- Kwa zaka zambiri m'Malawi muno alimi akhala akugwiritsa ntchito a tonde a mtundu wa mbuzi za Boer pokweretsa ndi mbuzi za chikuda pofuna kukuza mtundu wa za chikudawu. A tonde a mtundu wa Boer akhoza kugulidwa kwa alimi omwe ali nawo muno m'Malawi ndi kuwika m'makola athu komwe kuli mbuzi za chikuda. Pofuna kuchulukitsa mbuzi dziwani izi:

1. Mbuzi zabwino zimafuna chisamaliro chabwino, makamaka pakadyetsedwe ndi kuteteza ku matenda. Mbuzi za chilendo zimakhala zosazolowera kumaloko ndipo sichedwa kugwidwa ndi matenda amene amapezeka kuno ku Malawi.
2. Onetsetsani kuti mwathena a tonde onse a m'kholamo (achikuda) kapena achotsedwemo ndi kusiyamo achilendo kuti akwere mbuzi kuti mukhale ana achikaladi ozuka matupi ndi okula msanga.
3. A tonde azisinthidwa kuti asamakwere ana awo
4. Kutu izi zitheke, pafunika kuti alimi onse a mbuzi akhale m'magulu kuti azigwirizana zochita.

**Yankhani mafunso awa:**

Fotokozani njira za m'mene mungathetsere mabvuto awa: mufotokoze m'mene mungathanirane ndi munthu m'modzi-m'modzi ndi a pagulu:

- A komiti agwirizana kuti agula a tonde awiri a mtundu wa Boer kuti atukule mtundu wa mbuzi za chikuda. Mamembala agwirizana kuti athene kapena kuchotsa atonde a mbuzi za chikuda kuti mbuzi zawo zikweredwe ndi atonde a mtundu wa Boer basi.
- Pamene atonde a mtundu wa Boer agulidwa, papezeka kuti mlimi m'modzi amene ali ndi a tonde a chikuda wakana kuthena kapena kuchotsa atondewo. Ndipo ndi kosatheka kuti alimi enawo aletse kuti atonde amenewa asasakanikizike ndi mbuzi zawo ndi kumazikwera.
- Ndipo alimi amene adagula atonde a mtundu wa Boer aja abweretsa chidandaulo cha mlimi amene akufuna kulepheretsa chitukuko cha mbuzi zawo. Akufuna inuyo muumirize mlimiyo kuti athene kapena kuchotsa atonde achikudawo.
- Kodi mukhoza kuthandizapo bwanji pamenepa?


## Phunziro 5: Kuwenga ziboda

Zolinga za phunziroli:

Pomaliza pa phunziro ili wophunzira athe:

1. Kuzindikira ziboda zomwe zikufunika ku ziwenga
2. Kudziwa kuwenga ziboda za mbuzi ndi nkhozs mosazipweteka

- Sinthawi zambiri kuti ziboda za mbuzi ndi nkhoza kuti zimakula mosayenera kapena kukhota ayi.



Maonekedwe a ziboda: zina zoipa zina zabwino.

(Kuchokera m'buku lolembedwa ndi a FAO: "A manual for the primary animal health care worker")

- Ziboda zikakula kwambiri zimapangitsa kuti mbuzi kapena nkhoza zizimva ululu ndipo imadya pang'ono chifukwa cholephera kuyenda
- Mutha kuwenga zibodazi pogwiritsa ntchito chida chowengera kapena mpeni wakuthwa. Mukawenga ziboda zimabwerera m'chimake.
- Ziboda za ziweto zimafanana ndi zikhadabo zathu. Ngati muwenga mozikizira, chiweto chimamva kuwawa ndi kutaya magazi.
- Muziwenga **pang'onopang'ono**.
- **Lekani** ngati muona kuti payamba kutuluka magazi.

## **Phunziro 6: Matenda amene amagwira mbuzi ndi nkhosa**

**Zolinga za phunziroli:**

**Pomaliza pa phunziro ili wophunzira athe:**

- 1. Kudziwa za matenda omwe amakonda kugwira mbuzi ndi nkhosa muno m'Malawi**
- 2. Kudziwa zizindikiro za matenda amenewa**
- 3. Kudziwa njira zoyenera kutetezera kapena kuchizira ngati zilipo**

**Yankhani mafunso awa:**

Tchulani matenda omwe amagwira mbuzi muno m'Malawi? Tchulani zizindikiro za matenda omwe mwatchulawa? Nanga mutha kuteteza bwanji matenda amenewa? Nanga mutha kuchiza matenda mwanjira yanji? Nanga mutha kupereka ulangizi wotani kwa mwini ziweto?

## Matenda amene amagwira mbuzi ndi nkhosa muno m'Malawi

<b>Nyongolotsi/njoka za m'mimba</b>	Nyongolotsi/njoka za m'mimba zitha kuyambitsa matenda, mpwerere ndi imfa kwa mbuzi. Njoka za m'mimba zimaikila mazira m'matumbo omwe amatuluka pamodzi ndi ndowe. Mbuzi imadya mazirawa pamene ikudya udzu pomwe pagwera ndowe zija. Ndipo mbuzi zimayamba kudwala pamene mazira agogomola njoka za m'mimba m'matumbo mwa mbuzi.
Choyambitsa	Nyongolotsi zimatengedwa ku msipu pamene mbuzi zikudya. Zimakulira m'matumbo a chiweto ndi kuyambitsa matenda. Zimaikira mazira m'matumbo momwemo ndipo zimatuluka pamodzi ndi ndowe ndi kugwera pa msipu.
Zizindikiro	Mpwerere ndi kuonda Nyongolotsi zimabvuta kwambiri nthawi ya mvula pakati pa miyezi ya December ndi Malitchi. Ndi matenda obvuta kwambiri omwe amagwira mbuzi muno m'Malawi. Zitha kupha mbuzi zambiri. Ndi zoipa kwambiri kwa ana ambuzi kusiyana ndi mbuzi za zikulu.
Katetezedwe	Ngati mbuzi ndi zodyetsera m'khola la ukhondo, sizingathe kutenga nyongolotsi/njoka za m'mimba. Ngati phaka la khola limalola kuti ndowe zizigwa pansu, mbuzi sizingadyenso mazira a nyongolotsi/njoka za m'mimba. Ndipo zimakhala pang'ono m'mimba mwa mbuzi kapena mwa nkhosa. Kusunga mbuzi molingana ndi kukula kwakhola kumachepetsa kufala kwa njoka za m'mimba. Mbuzi zachilendo ndi zimene zimatenga kwambiri njoka za m'mimba
Kuchiza	Mankhwala alipo ophera njoka za m'mimba. Ena ndi odyetsa, ena omwetsa ndi ena obaya - onsewa amagwira ntchito bwino.



<b>Mkupe</b>	Mkupe ndi matenda ogwira pakhungu la chiweto. Ndipo amanyerenyetsa., ndikupangitsa kuti khungu likhale lokhakhala ndipo chiweto sichikula bwino. Matendawa amafala ndi mbuzi zimene zikudwala matendawa pamene zisakanizana ndi mbuzi za thanzi.
Choyambitsa	Tinsabwe tating'ono kwambiri timalowa m'khungu ndipo mbuzi zimamva kunyerenyetsa kwambiri.
Zizindikiro	Kumeteka bweya ndipo zipere zokhakhala zomaoneka. Izi zimakonda kuoneka m'mutu, mkhosi, ndi pamsana pamene pamaoneka ngati pali mamba. Ubweya umachoka ndipo khungu limakhakhala
Kuchiza	Mankhwala a mtundu wa dibi osambitsa ndi othira pansana alipo. Mankhwala awa amapha tinsabwe. Palinso mankhwala obaya otchedwa <i>ivermectin</i> amene amagwira ntchito bwino.

<b>Matenda a maso</b>	Awa ndi matenda ogwira m'maso. Maso amaoneka ofiira kapena otuwa. Chiweto chimamva kupweteka ndipo chingathe kuchita khungu. Chiweto sichitha kudywa bwino ndipo chimalephera kukula bwino matenda amaso amafala pamene mbuzi zodwala matendawa zisakanikilana ndi zathanzi.
Choyambitsa	Kachiroambo ka mtundu wa <i>bacteria</i> kamafalitsidwa kudzera ku fumbi ndi ntchentche kuchokera kuchiweto kupita kuchiweto china.
Zizindikiro	Maso amafiira ndi kutupa. M'maso mumatuluka misozi yambiri. Maso amaoneka otuwa ndipo mumatuluka manthongo. M'maso mumatuluka zilonda nthawi zina. ziweto zambiri zimachira opanda mankhwala. Komabe, zimatha kupatsira matendawa ku ziweto zina zamoyo nthawi imene abuka matendawa.
Katetezedwe	Kuthetha ziweto zodwala kumathandiza kuchepetsa kufalitsika kwa matendawa.
Kuchiza	Mankhwala a ufa kapena amafuta amapezeka othira m'maso.

<b>Chibayo</b>	Chibayo chimagwira mapapo. Chiweto chimadwala kwambiri kapena kufa ndi chibayo. Mbuzi zomwe zikudwala matenda a chibayo zitha kufalitsa matendawa ku mbuzi za thanzi pamene zikutsokomola kapena pamene zikhalila malo amodzi.
Choyambitsa	Kachirombo kakang'ono ( <i>germ</i> ) kamalowa m'mapapo ndipo kamapangitsa kuti chiweto chizilephera kupuma bwino ndipo chimafa
Zizindikiro	Mbuzi imaoneka yodwalika ndipo imatuluka mamina m'mphuno, misozi m'maso, imachita befu, kutsokomola, ndipo kenaka imafa.
Katetezedwe	Kukhetha mbuzi zonse zodwala pofuna kuteteza kupatsira matendawa kwa zamoyo. Mbuzi zikhale m'khola limene lingateteze mbuzi kumphepo ya mkuntho, yozizira, ndi mvula.
Kuchiza	Mankhwala alipo opha tizilombo toyambitsa matendawa monga ngati <i>oxytetracycline</i>

<b>Kafulukutu (kuola kwa m'ziboda)</b>	Awa ndi matenda owoletsa ziboda. Amayambika ndi kachilombo kosaoneka ndi maso ndipo amafalika kuchokera kuchiweto chodwala kupita kuchiweto cha thanzi maka pamalo pamene pali pachinyonho ndi matope.
Choyambitsa	Kachirombo kakang'ono ( <i>germ</i> ) kamalowa ku ziboda ndi kuziononga kupangitsa chiweto kupunduka
Zizindikiro	Kafulukutu amakonda kugwira ziweto pamene ziweto zikhala pamalo a chinyonho ndi a matope. Matendawa ndi oipa chifukwa amapangitsa chiweto kukhala chopunduka.
Katetezedwe	Ziweto zisakhale nthawi yaitali pamalo a chinyonho ndi a matope Zikhale m'khola louma maka lam'mwamba ndiye labwino. Khethani mbuzi zodwala matendawa kuti zisapatsire matendawa ku za moyo.
Kuchiza	Mankhwala alipo ochizira matenda amenewa Pali mankhwala omwetsa kapena kubaya ophera tizirombo toyambitsa matendawa monga: <i>penicillin</i> , <i>streptomycin</i> , <i>tetracycline</i> , ndi ena opaka pazilondapo amapezeka. Ngati ulimi wambuzi ndi wodyetsera m'khola, pali mankhwala othira pachidekwe chomangidwa ndi simenti pakhoma podutsa kuti aliyense olova m'khola azibviika mapazi m'menemo. Ena mwa mankhwalawa ndi: 5% <i>copper sulphate</i> , 10% <i>zinc sulphate</i> , 5-10% <i>formalin</i>

<b>Zotupa</b>	Awa ndi matenda ogwira khungu amene angafalike kuchoka kumbuzi ina kupita kumbuzi ina maka nyengo ya mwamvu.
Choyambitsa	Kachirombo kakang'ono ( <i>germ</i> ) kamalowa m'khungu la chiweto. Kachiromboka kamachokera ku ziweto zomwe zagwidwa kale matendawa.
Zizindikiro	Chiweto chimamva kunyerenyesa ndipo chimatuluka matuza okhala ndi nkhanambo, maka ku mphuno, kunkhope, pamphuno, m'makutu, kumabvalo ndi m'ziboda. Zimayamba ndi zotupa zolengeza mafinya olimba pakhungu, kenaka ndi kusanduka nkhanambo zooneka mwachikasukasu. Nkhanambo izi zimakhala zosongoka ndi zolimba mukazigwira ndipo ubweya umasosoka pamalopo. Matendawa amakonda kugwa nthawi ya mwamvu ndi malo achinyontho kumene kuli tizirombo ndi nkhopakupa zambiri. Matendawa amagwa kwambiri nyengo ya mwamvu kusiyana ndi nyengo ya chirimwe
Kuchiza	Mankhwala akumwa ophera tizirombo toyambitsa matendawa alipo.

<b>Matuza otuluka m'mphuno ndi mkamwa (orf)</b>	Awa ndi matenda odziwika bwino amene amatulutsa matuza pakamwa m'milomo ndi mkamwa mwa mbuzi.
Choyambitsa	Kachirombo kamtundu wa virus kamene kamafalitsidwa ndi ziweto zina zomwe zikudwala matendawa. Kachiromboka kamalowera m'mabala omwe ali pakungu la chiweto omwe amadza chifukwa cha minga, ndi zina zotero.
Zizindikiro	Matendawa amayambitsa matuza m'milomo, m'mphuno ndi pamphuno. Nthawi zina amakafalikira kubere. Matuza amatuluka othinana amtundu wotuwa kenaka amauma ndipo amakhala okanika kuchotsa. Matendawa amagwira ana a mbuzi ndi nkhoa a misinkhu ya miyezi yapakati pa itatu kufika isanu ndi umodzi. Matendawa akhoza kugwiranso munthu. Ziweto zimachira pakati pa masabata awiri ndi atatu. Ziweto zomwe zagwidwa matendawa sizitha kudyana ndipo zimaonda.
Kuchiza	Ziweto zimene zagwidwa kwambiri zimafunika kumazidyetsa ndi manja mpaka zitachira. Njira yochita kudyetsayi imathandiza ziweto pamene zapezeka ndi matendawa ndipo zikulephera kudyana zokha. Mankhwala osambitsa ophera tizirombo toyambitsa matendawa alipo.

## **Mafunso apomaliza pa maphunziro a gawo**

1. Kodi anthu amaweta mbuzi muno m'Malawi pa zifukwa ziti?
2. Nanga ndi zifukwa ziti zobvuta zomwe alimi amakumana nazo pa kawetedwe kambuzi?
3. Jambulani khola la mbuzi la m'mwamba ndi kusonyeza utali wochoka pansi kufika pa phaka, ndi kusalika kwa nkomo za m'mbali mwakhola.
  - Kodi mbuzi imodzi yaikulu imafuna malo akulu bwanji?
  - Nanga kutsetsereka kwa denga la khola kukhale kotani?
4. Tchulani mtundu wa zakudya zoonjezera zimene mungadyetse mbuzi panthawi yoti zakudya zikusowa.
5. Tchulani mitundu ndi ntchito ya mbuzi zomwe zimapezeka m'Malawi muno.
6. Kuswanitsa mbuzi:  
Tchulani zizindikiro zakuti mbuzi yayamba nyere  
Pamatenga nthawi yaitali bwanji pamene nyere yatha ndipo kuti iyambenso yina?  
Nanga nyere yambuzi imatenga nthawi yaitali bwanji kuti ithe?  
Nanga bere lambuzi limakhala nthawi yaitali bwanji isanaswe?  
Nanga msoti wa mbuzi umatha msinkhu uli waukulu bwanji?
7. Kodi ndi njira ziti zomwe alimi angatsate pofuna kutukula mtundu wa mbuzi za chikuda pokweretsa ndi a tonde a mtundu wa Boer?
8. Ndi nyengo iti imene nyongolotsi kapena njoka za m'mimba zimabvuta kwambiri ku mbuzi?  
Nanga mukhoza kudziwa bwanji kuti mbuzi zanu zili ndi nyongolotsi kapena njoka za m'mimba?  
Tikhoza kuchiza bwanji matenda a nyongolotsi kapena njoka za m'mimba ku mbuzi?
9. Matenda a chibayo amaonetsa zizindikiro ziti ku mbuzi?  
Nanga tingachize bwanji matenda a chibayo?